

## **Bukhu Lakafukufuku Mwachidule pa Purogaramu yapa Wailesi ndi Greg Anthony pa Wailesi ya First Amendment August 7, 2014**

Greg anayamba ndikuti Tony Alamo ali mundende kuyambira 2008 kwa zaka 175 pamilandu yongonamiziridwa ya kugwilirira, ndi mmene Tony, pazaka 40 mpaka 50 zapitazi, wakhala akutiuuzira zonna zokhudzana ndi mchitidwe wa Vatican onyengelera anthu pa zaufulu wathu wa chipembedzo ndi njira zankhanza zolowera mu dongosolo lathu la ndale.

Analongosola za momwe Tony akufikira anthu zikwi zikwi kuzungulira dziko lonse ndi nkhani imeneyi yosagwirizana ndi Vatican yomwe ikuyenera kunenedwa chifukwa pali chiyembekezo cha umboni wa chimene chinayambitsa chowonetsa kuti zimene Tony akunena ndizoona, ndipo akuyimbidwa milandu chifukwa cha chimenechi.

Greg ananena za nkhondo ya 2008 ku Arkansas, kuti inali ngati sitailo ya nkhondo ya mzinda wa Waco pa utumiki umenewu umene anaumva kuchokera m'malo akuluakulu ofalitsa mauthenga amene amaoneka kuti akudziwa zambiri za utumikiwu. Akuganiza cholinga chawo chinali kuthetsa utumiki opambana kwambiriwu umene unali ndi matchalitchi m'maboma angapo osiyanasiyana, komanso kulimbana ndi Tony. Mmene anapangira kunali kufuna kulimbana ndi ana a utumiki umenewu. Anafananiza ndi zimene ananena wina wake pa bulogu yake za nkhondo: pamene maofesala a boma ndi chitaganya okakamiza kumvera malamulo (state and federal law enforcement) anafika mwadzidzi mu Tony Alamo Ministries, ambiri, ngati asali paupifupi onse, mwa malo akuluakulu owulutsira nkhani anali ku Texarkana, Arkansas, kuonelera zonse zikuchitika, koma osalemba kalikonse ka izo kufikira zitayamba kale. Kotero amadziwa zonsezi. Nkhondo inakhanzikitsidwa kuti iyambe mu October, koma nkhondo imeneyi inayamba msanga mu September. Lachisanu, tsiku lakuti nkhondo iyamba mawa, wina wake mu Ofesi ya Oyimira anthu pa milandu, Attorney, ku US, mosachita kufuna anatumiza imelo yokamba za nkhondo kumalo ofalitsa nkhani oposa 50 m'boma lonse. Imelo imeneyo inatumizidwa milungu yambirimbiri nkhondo isanakondedwe kuti ichitike. Greg akukhulupilira kuti unali msampha omupezera zifukwa Tony asanapatsidwe chigamulo chachilungamo.

Frank Lockwood pabulogu yake ananena izi: "Chinsisi chitafululika maofesala owona zamalamulo anawonjezera nthawi yamapulani awo. Munyuzipepala amayeneleka kupanga chisankho pakati moyilemba nkhani mu edishoni ya loweruka kapena kudikira tsiku limodzi kapena awiri. Ana zitalengezedwa kuti ali mutchalitchi, komanso ndi nkhani zabodza zochitira ana nkhanza, bungwe lililonse lofalitsa nkhani m'bomalo pailo lokha linasiya kulemba za nkhondo yadzidzidzi kufikira itayamba kale." Zimenezi zinawasangalatsa kwambiri ofalitsa nkhani; palibe amadziwa chenicheni chimene chimapangika. Ndi zopweteketsa kupezeza ndi mulandu itangochitika kumene nkhondo yotutumutsa munjira yosayembekezera. Analongosola za momwe gulu ladzidzidzili linabwelera litatenga mfuti, kuwapatsa mantha, pamene ana anali kusewera panja, kuyesera kumumanga Tony, koma Tony kunalibe, anali ku Los Angeles panthawiyi. Panalibe zizindikiro zosonyeza kuti panali zida zankhondo kapena chilichonse patchalitchipo. Linali bungwe la bata ndi mtendere, ndipo ngati amafuna kumumanga Tony, akanatero mwakachetechete, koma izi zinali zoysa munkhani, ndipo inali njira yomumangira isanafike nthawi yokhala ndi chigamulo chopanda chinyengo.

Ana asanu ndi m'modzi anasungidwa mmanja mwaboma tsiku limenelo. Tsiku lotsatira, nkhani inatuluka m'malo monse motchuka mofalitsira nkhani. Anthu ambiri m'dzikolo, ndi Tony Alamo anali atamangidwa kale. Nkhani imeneyi inayikidwa pa Oprah Winfrey ndi ena mwa matchanelo akuluakulu a milandu.

Greg ananena kuti malinga ndi maloya, iwo alibe zambiri panopa, ndipo zomwe ali nazo zikanasokonezedwa. Uwu ndi mulandu wongowopseza kukuwonetsani zimene angakuchitireni ngati mungaganize zotsutsana ndi tchalitchi cha Katolika ndi Vatikani. Greg analongosola za momwe United States imabisira makhalidwe ake oipa, umthira kuwiri, kuloleza matchalitchi a Vatikani kukhala omasuka pambuyo pokhala ndi umboni wambiri wa zimene zimachitikira ana m'masukulu ku Canada, ku Ireland, kuzunza ndi nkhanza pa dziko lonse lapansi, ndipo tikulolabe tchalitchi kuti chiziyendabe?! Iwo ali ndi ndalamo komanso mphamvu ndikuyendetsa boma lathu ndicholinga chobisala ku nkhanza zomwe amapanga zonzuza ana. Ngati muli ndi mawu okwenza ngati a Alamo, akhonza kukupachikani ndi milandu yofanana ndi imene iwovo anapezeka nayo olakwa ndikugwiritsa ntchito owulutsa nkhanzi, FBI, owona za malamulo kuti akutsatiridwa, ndi ziphuphu, komanso pakukakamiza anthu kubweretsa milandu yabodza kenako ndikusiya chikhulupiliro chawo chakale ndikuyamba kumvera iwo. Ananena za mlandu wapachiweniwi mu March komanso za chigamulo cha madola theka la biliyoni.

Greg anafotokoza za Tony kuti ndi wachikulire wazaka 79 zakubadwa ndipo ndiwakhungu mundende. Kenako anakumbukira ndikubwerenza kunena zimene Tony ananena kuchokera kundende: kwa zaka pafupifupi makumi asanu, akhala akuyesayesa kundichotsa. Koyamba, anatinamizira kuti timagwirizana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito chinthu chimodzi anthu ambirimbi, anativutitsa ndikutitsekera mundende pamodzi ndi mamembala athu osalekeza ndicholina chotilepheretsa kuchita zomwe tikufuna komanso kusiyitsa mkazi wanga Suzana ndi Ine kulalikira choonadi cha Mawu a Mulungu. Kenako anafuna kuti tikhale a Waco, ndikupitiliza kutinamizira kuti ndife a chipembedzo choopsa komanso zigawenga zokhala ndi zida zowopsa. Kenako ndinanamiziridwa zopangira ana nkhanza zimene milandu yake inathetsedwa ndi Loya wa Boma waku Los Angeles. Kenako anawopseza zokuba oweruza milandu wa Federal. Gulu la anthu losankhidwa kuti limvere mlandu m'bwalo la malamulo ndikupereka maganizo awo pa mlanduwo anandipeza osalakwa. Kenako IRS inagwiritsidwa ntchito kupanga mlandu wabodza osapereka ziphaso pa phindu limene silinakhalepo. Loya wanga, Jeff Dickstein, wotsutsana ndi zaziphaso, anayikidwa pa mpanipani pofuna kundipereka kapena kupita kundende iyeyo. Ndinagamulidwa zaka zisanu ndi chimodzi, ndipo ndi nthawi yabwino, ndinatuluka muzaka zinayi mchaka cha 1998. FBI inapitiriza kundifufuza opanda kufowoka. Pomaliza, m'chaka cha 2008, anapeza mboni zabodza zingapo zimene zinasiya mpingo zaka zambiri zapitazo ndikulolera kuvomelezana nawo. Ntchito yopereka zinthu kwamwini zomwe zinatayika kapena kubedwa komanso ndalamo m'mlandu wapachiweniwi inali yonyengelera kwambiri. Pamlandu wapachiweniwi anagwiritsa ntchito mboni zisanu zomwezo ndi wachisanu ndi chimodzi, yemwenso anali membala kale amene anagwiritsidwa ntchito pamulandu wopalama, kuti athandize mulanduwo. Koma nthawi imeneyi munkhani yobweretsedwa kubwalo la milandu, Civil Suit, ankafuna kulandira dipo la ndalamo koteri anapeka bodza lina loti ankamukonzeretsa kukhala mkazi koma anathawa kaye. Wachisanu ndi chimodzi anali mutchalitchi mpaka June, 2010, akudziwabe kuti ndinali osalakwa ndikundithangatira mlandu utatha. Kenako anachoka mu June. Pofika August anali atalowa Civil Suit chifukwa chofuna ndalamo. Civil Suit inali mukhoti la federal, koma kuyandikira mlandu, Oweruza pamapeto anayankhula za maganizo a chiweruzo mwachidule amene anaperekedwa, ndipo milandu yonse inathetsedwa. Kotero kuti mulandu unatsekeda ndipo kenako unakatsekulidwanso kukhoti la boma la Arkansas. Oweruza anavomereza milandu yonse imene anayichotsa kuti ibwelere mukhoti la boma. Tinalibe ndalamo zolimbananso ndi mulanduwu, koteri zinatipangitsa kuti tiluze.

Greg ananena kuti anamuchita chiwembu Tony ndi tchalitchi pamene panawapweteka kwambiri: ana. Anafufuza aliyense wam'mautumiki ake za ana ena amene sanatengedwe munkhondo yadzidzidzi yoyamba. Analongosola za nkhondo yadzidzidzi yoyamba ndi maofesala apolisi 100, gulu la swat, ndi momwe anakwatulira atsikana asanu ndi mmodzi omwe amachita masewera ozendewera. Panalibe ndi mmodzi yemwe mwa atsikanawo amene zinatsimikiza kuti ali ndi chili chonse chosakhala bwino chokhudzana ndi Tony.

Anawakhwekhweleza ndikuwaponya mungolo ndikunka nawo atsikanawo akuyimba nyimbo za uzimu. Analongosola za mafunso othandiza a khoti ndi a polisi kuti apeze anthu achifwambawo amene anachitika tsiku lotsatira ndi atsikanawo, analongosolanso za mmene sanapezele kanthu, ndi mmene mmodzi mwa atsikanawo anali m'chemwali wa wachikulire amene amakhala pamenepo, koma anakanabe kukamupereka kwa makolo ake. Department of Human Services inasunga atsikana asanu ndi mmodziwo, ngakhala sanapeze chovuta chili chonse, ndipo oweruza analamula kuti mwana aliyense adzatengedwe mutchalitchi kumalokeshoni onse aku US.

Mpingo unathawa ndi ana awo ndicholinga chongothawa – njira wabwino yobalalitsira zinthu. Ananena za momwe mavani awiri a ana anayimitsidwira pamsewu waukulu. Anakwatula makanda ndi ana osawaperekanso. Greg anati kumeneko ndikuba ana. Iye anabwerenzanso kunena kuti sanapeze kuvulazidwa kwa mtundu uliwonse pa anawo, ndipo palibe chinapezeka chompezera chifukwa Tony chimene akadagwiritsa ntchito pamlandu wake, monga momwe amaganizilira. Anadziwa kuti inali njira yowonongera utumiki wake wonse. Greg kenako anafunsa ngati ili linali dziko la Gestapo. Greg anati izi zinachitika ndi cholinga chothetsa utumiki umenewu, kuletsa Tony kuti asayankhule zotsutsa Vatican, ndikutenga katundu yense wa Tony ndi ndalamala zake zonse. Greg anafunsa, “Ndichifukwa chiyani osangotenga ndalamala zonse kuchokera ku Vatican pa zonse zimene apanga?” Panali mlandu wakukhoti wokhudzana ndi zimenezi ndipo iwo ananena kuti, “Vatican siyimapanga malonda ku Amereka.”

Anayesayesa kugwetsa utumikiwu powamwaza anthu amene amakonza zotayipa, kupurinta, ndi kugawa zolembedwa/mabuku, ndi amene amayendetsa utumikiwu kumizinda yamu US yonse mulungu uliwonse, kugawa mabuku ndikutumiza. Greg analongosola za mabukuwa kuti ndi zimene amayankhula pa porogaramu yake, makopedwe a Vatican pa ufulu wathu wa chipembedzo ndi pa boma lathu ndikukhulupiritsa aliyense kuti iwo ndi tchalitchi chokhacho chowonadi. Ngati pali chipembedzo chaupandu, ndi Vatican! Greg ananena kuti makolo anali ndi chisankho chokhumudwitsa kwambiri chosiya utumikiwu kapena kuluza ana awo, ndikuluza ufulu wawo ngati makolo. Chisokonezo cha ana ndi makolo chikuyika utumikiwu pakatikati osapita m'tsogolo. Kenako ana anapusitsidwiratu ndikukhala amphulupulu ndi osamvera makolo awo, komanso kuwada pamodzi ndi tchalitchi chimene ankachikonda.

Funso limene Tony akufunsa kuchokera muchitokosi chake mundende nali: “Pamene pali umboni okwanira kuti m'chipembedzo chaupandu cha Katolika amachita nkhanza kwa ana, ndichifukwa chiyani ana sakuletsedwa kupita ku sukulu zawo, matchalitchi awo, malo osungirako ana amasiye, nyumba zokhalamo akazi osakwatiwa okhudzana ndi zopemphera, ndi ena ambiri? Ndichifukwa chiyani makolo a Katolika amene anatumizanso ana awo m'chipembedzo chaupandu chozunza anachi tsiku lililonse sakulandidwa mphamvu ngati makolo komanso ana awo kutengedwa?”

Greg analongosola za nkhanzi ya momwe mai ake anamwalilira ndi nthenda ya leukemia pamene m'chimwene wake wa mng'ono amene anabadwa masiku osawkana anali ndi miyezi isanu ndi umodzi yakubadwa ndipo abambo ake anali ndi mabilu ankhaninkhani oti alipire. Panali malo osungirako ana amasiye a Katolika pafupi ndi kumene amakhala kumene amabweretsa ana onsewa. A monsignor anabwera kunyumba kwake, koma mmalo mopereka

thandizo kwa bambo ake a Greg, amafuna atenge ana kuchoka kwa bambo ake ndikukawayika kumalo osungirako ana amasiye a Katolika. Abambo ake anawagwira a Monsignor ndikuwavukuzira kukhoma, kuwakankhira kunja, ndikuwagwetsera pamasitepe. Greg anati, "Ndim'mene ndikumvera za Vatican. Kuwamenya m'matako ndikuwathamangitsa m'nyumba mwako. Ndizimene anachita bambo anga, ndipo tinakula ndi moyo wathanzi komanso osangalala, ndipo m'chimwene wanga panopa ndi wabizinesi yochita bwino kwambiri." Bambo ake analumbilira kuti sadzapondetsanso phazi lawo mutchalitchi cha Katolika, zimene sanachitedi. Ndipo sanamutumize m'chimwene wake wam'ngono ku sukulu ya Katolika. Bambo ake anafunsa Greg kuti awalore kumuchotsa ku sukulu ya Katolika, koma Greg anawapempha kuti akhalebe konko chifukwa anzake anali komweko ndikuti amai ake anali atangomwalira kumene.

Mutheka lachiwiri, Greg ananena za ndende zimene Tony wakhalamo ndi mmene anaunikilira kulumikizana konse ndi mmene zimakhalira podzamuona; palibe chinsisi chili chonse. Boma linalipira Cult Awareness Network ndalamala madollar oposa 5,000.00 za aliyense mwa mboni zitatu zotsutsana ndi Tony ya chiphunzitso chimene anali nacho kwa milungu iwiri chowazamitsa kukanama motsutsana ndi Tony chimene chinachitikira kudera kosatukuka kotchedwa Wellspring Retreat. Boma linawalipira maulendo onse amene ankayenda komanso linalipira \$1,500.00 ya mwana wa m'modzi mwa mboni kuti aziyang'aniridwa pamene mai ake ali m'chilangizo. Analipira mbonizi ponamizira kulipira mabilu amene sangakwanitse kugwira ntchito kuti alipire ali kumeneko, monga chiteteko cha galimoto, ndi zina zambiri. Wankulu oyang'anira wakale wapa Wellspring, Paul Martin, iye mwini anagwira ntchito pa mboni zimenezi. Zinachitika mu December m'chaka cha 2008, ndipo izi zitangotha Bambo Martin anagwidwa ndi matenda, anapezeka ndi leukemia ndipo anamwalira patatha miyezi yambiri.

M'mbuyomu, umboni wa amene anasulidwa kuchita bodza ku Wellspring unachotsedwa kukhoti. Koma ngati aliyense oyimbida mulandu angayankhule ndi mboni, akhonza kuzengedwa mulandu osokoneza mbonizo. Pomwe boma likhonza kuzitengera mbonizi kumalo amenewa kukawazamitsa pakukhala owukira. Anthu akhonza kuitako alibe mbali yomwe akutenga ndikukabwerako otsutsa kwambiri. Ndi mfundo yofunikira kwambiri m'mulandu umenewu.

Anati Dorothy Curry ananena kuti *Unsolved Mysteries* inanama, ndipo kuti Tony Alamo sanazunze mwana wake wamng'ono. Iyi inali 1991 pamene amayesera kupanga zomwezo kwa Tony, koma osakwanitsa. Greg anawerenga zina mwa zimene Dorothy ananena muzolembewazo pamene anakana zimene Jim Griffin ananena zakuti Tony anamupanga nkhanza Carissa.

Greg anawerenga nkhanzi mu *Protestant Mission Newsletter* ya British Columbia yamomwe abale a muutumikiwu anapitira ku Canada ndikukagawa mabuku a Uthenga Wabwino pamene Papa Yohane Paulo Wachiwiri ankapitako. Tsiku limene Papa anafika, abale anamangidwa. Sanayimbidwe mulandu uliwonse, sanapereke zifukwa, koma anawasunga mundende mpaka tsiku limene Papa ananyamuka ku Canada pamene anamasulidwa osalongsola kalikonse ngakhale kupepesa. Greg anapitilira kunena kuti mlambi wa nkhanzi anati amadziwa kuti kugawa mabuku kuyika poyer a mchitidwe wa Roma Katolika ndi chifukwa chenicheni Tony Alamo anamangidwanso. Amaudindo akuluakulu amene ali ndi mphamvu zolamula akuyesetsa kupeza mboni zachinyengo. Ngati amaudindo akukhudzika kwambiri ndi ana kuti akuchitidwa nkhanza komanso kugwiliridwa, bwanji sakutseka mabungwe onse a Roma Katolika poti ndizodziwikiratu kuti ana masauzande ambirimbi (Greg anawonjezera kuti mahandiredi amasauzande, mamiliyonu m'zaka zadutsa) akhala akuchitidwa nkhanza

zowagwililira ndi zapathupi, kuzunzidwa, komanso kuphedwa kumene ndi ansembe osakwatira a Katolika? Iye anafunsa, “Ndikangati kamene munamva za wamsembe akuyimbidwa mulandu ndi m’modzi mwa anthu amene amawagwililira kapena kuwachita nkhanza, kuyembekezera chilungamo, koma ndikupeza kuti munthu okonda chiwerewereyu amusamutsira kunyumba ina yokhala anthu a chipembedzo opanda mabanja, monasteri, kapena tchalitchi china mwachinsinsi kuti akapitilize za nkhanzazo ku malo kwina? Kodi chilungamo chili pati? Zikutheka bwanji makolo a Katolika amene akudziwa ndikale za ansembe kuti amazunza ana koma nkumatumizabe ana awo kwa anthu okonda kuchita chiwerewere ndi ana ang’onoang’onowa? Kodi chikhalidwe chawo cha umumthu ndi chikondi chili pati? Kodi kumeneko sikulekelera? Akudziwa ndipo akhonza kuwerenga za m’chitidwe wa anthu okonda kuchita chisembwere ndi ana achichepere mumanyuzipepala tsiku ndi tsiku. Ndichifukwa chiyani amaudindo olamula sakukhudzika ndi mphete yayikulu ya nkhanza zogwililira ana? Pali kukoma kwa uku ndi uku, kwina kwa Rome, ndipo kwina kwa dziko lonse lapansi monga mwa nkhanzi ya Tony Alamo.”

Greg anawerenga zina zake zolembedwa ndi mzibambo wotchedwa Shane m’chaka cha 2009 amene amatchula DHS dipatimenti ya mavuto a munthu. Ananena kuti DHS inaba ana 35, kuyika mundende Tony Alamo, ndipo pakutero, ndikuyika Baibulo pamayesero. Utumiki wa Alamo sichipembedzo cha upandu kapena choipa ayi, koma gulu lokhulupilira Baibulo lachiKhristu ndi lamtendere lokonda kulalikira za Baibulo padziko lonse lapansi. Chifukwa chosamveka bwino chimene oweruza anaperekwa potenga anawa kwa makolo awo ndichakuti sanabayidwe katemera komanso sanalembetse ndi boma ngati ophunzilira pakhomo. Kenako Greg ananena kuti iwo akhonza kuyika kachirombo ka Ebola mujakisoni, koteri atalikireni ndi akatemera a chinfine. Iye anati akhala akutseka ena mwa mawebusaiti otsutsana ndi katemera. Shane anati chilungamo chenicheni cha kuba ana kumeneko ndichakuti mautumiki a Alamo amalalikira “BABULO WACHINSINSI WAMKULU, MAI WA ACHIGOLOLO NDI ZONYASITSA ZADZIKO” (Chivumbulutso 17:5).

Greg anati ndi chifukwa chimodzi chokha chimene anagwilira Tony ndipo ndichakuti ndiwochita bwino kwambiri. Utumiki wake ndiwotchuka kwambiri, zedi, ndipo uthenga wake umafikira anthu masauzande ndi mahandiredi amasauzande. Ngati anakhala mnyumba mwake kuyankhula kwa anthu 20, sakanavutika naye, koma sakufuna kuti chinsisi chawo chiululike, ndipo ndi chifukwa izi zinamuchitikira. Njira yake sikukhulupilira kokha zomwe mwamva kuchokera kumalo ofalitsa nkhanzi otchuka pa nkhanzi iyi chifukwa sanakuuzeni za mchitidwe woumiriza anthu kuchita zinthu powaopseza; sanakuuzeni za zinthu zambiri. Anamupezera milandu ndikulankhula za nkhanzi ngati ozenga milandu anthu owononga, ndipo aliyense wakuyimvera ankachokapo ndikumati, “Wayenera kukhala wolakwa.” Ndimomwe boma, ofalitsa nkhanzi, ndi Vatican amagwilira ntchito limodzi.